# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA SALIMA M'DZINJA LA 2024 -2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya mvula ya 2024-2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira koposa mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.
Boma la Salima likuyembekezeka kulandira mvula yochulukirapo kuyerekeza ndi chaka chatha ndipo ikhala ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.

## October 2024




Mu mwezi wa October madera ena a boma la Salima akuyembekezeleka kudzalandira mvula yochepa kwambiri ya chizimalupysa ya mlingo wa 15mm. Tiyembekezere kuti mvulayi idzabwera ndi mphepo ya mkuntho ndi mvula ya mabingu kamba ka kutentha kwambiri mu mweziwu.


## November 2024




Mlingo wa mvula yosaposera 50mm ukuyembekezereka m'bomali m'mwezi wa November.


Tiyembekezere nyengo yadzinja kuyamba pakati pa sabata yomaliza ya mweziwu ndi sabata yoyamba ya mwezi wa December. Koma m'madera ena nyengo yadzinjayi ikhoza kudzayamba m'sabata lachitatu la mwezi wa December.

## December 2024




Mu mwezi wa December, mvula ya mlingo osaposera 200mm ikuyembekezereka m'madera ambiri m'bomali. Koma madera ena ozungulira SC Msosa ayembekezere mvula ya mlingo wapafupi fupi 220mm.
Mvulayi ndi ya mlingo okhazikika wa mwezi wa December.


## January 2025




Madera ambiri akuyembekezeka kudzalandira mlingo wa pakati pa 200mm ndi 300mm. Koma yoposera mlingo wa 350mm idzagwa madera ena ozungulira TA Ndindi ndi TA Kuluunda .

Chiopsezo cha ng'amba yoposera sabata imodzi mu mweziwu ndichochepa m'bomali.


## February 2025




Boma la Salima likuyembekezeka kudzalandira mvula ya mlingo 200mm ndi 300mm omwe ndi mlingo okhazikika. Koma mvula yochulukirapo idzagwa makamaka madera ozungulira TA Maganga.


Tiyembezere ng'amba yoposa sabata imodzi mu mweziwu.

## March 2025




Madera ambiri ayembekezere mvula ya mlingo wa pakati pa 150-250mm m'mweziwu, koma mvula yochuluka ya mlingo wa 300mm idzagwa m'madera akwa TA Kuluunda ndi TA Maganga.
M'madera ena nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kupita kumapeto mu sabata lachitatu la mwezi wa March kufikira sabata lachiwiri la mwezi wa April.

## April 2025





Pomwe nyengo ya dzinja idzakhale ikupita kumapeto, boma la Salima likuyembekezera kudzalandira mlingo wosaposera 50mm.

M'madera ena nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kupita kumapeto pomafika mu sabata lachitatu la mwezi wa March kufikira sabata lachiwiri la mwezi wa April.

Mvula yodzalila ikuyembekezeleka pakati pa sabata yomaliza ya November ndi sabata lachitatu la mwezi wa December 2024. Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kudzafika kumapeto m'sabata lachiwiri la mwezi wa April. Koma madera ena nyengo yadzinja idzatha mu sabata lachitatu mwezi wa March 2025. Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kudzakhala ya masiku apakati pa 110 mpaka 130. Ng'amba yotalika kuposera sabata limodzi ikuyembekezeka mu mwezi wa February 2025.
Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.

| SALIMA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.1 | 4.9 | 11.2 |
| NOV | 14.3 | 38.5 | 26.8 |
| DEC | 159.3 | 295.6 | 190.4 |
| JAN | 204.6 | 407.1 | 323.8 |
| FEB | 199.4 | 327.9 | 309.8 |
| MAR | 159.8 | 271.6 | 353.8 |
| APR | 27.3 | 62.6 | 79.7 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre. Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79
Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website:
www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com